## UNDUNA WA ZACHILENGEDWE

## NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## NYENGO MSABATAYI

Kuyambira Pa 20 mpaka Pa 26 July, 2026

### NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

Kuyambira Lolemba mpaka Lachisanu, tiyembekezere nyengo yopanda mitambo komanso yozizira usiku ndi m'mawa madera ambiri. Kudzikhala nyengo yofunda komanso yadzuwa nthawi ya masana. Izi zikhala chonchi kamba kadera la mpweya olemera omwe wakhazikika pamtunda omwe ukukanikitsa kapangidwe ka mitambo.

Kuyambira Loweruka mpaka Lamulungu kudzakhala nyengo ya mphepo komanso yamitambo ndi mvula yamawawa komanso yowaza m'madera ochepa kamba ka mphepo za chinyontho chochuluka kuchokera ku m'mwera chakumvuma m'nyanja ya mchere ya India.

Mphepo ya mphamvu ya Mwera ikuyembekezeka kudzaomba pa nyanja ya Malawi ndi nyanja zina kuyambira Loweruka, choncho asodzi ndi ena onse ogwilitsa ntchito nyanjazi akhale osamalitsa.

### NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

M'sabata yangothayi m'madera ambiri kunali kopanda mitambo, kozizira kwambiri komanso chifunga nthawi ya usiku ngakhalenso m'mawa. Masana, kunali kwa dzuwa komanso nyengo yofunda ndi ya changululu.

Madera ambiri kunazizira kuposera mlingo okhazikika wa mwezi wa July, maka nthawi ya usiku ndi m'mawa. Komwe kunazizira kwambiri kunali ku Katete Forest ku Lilongwe ndi mlingo wa 2.9°C pa 17 July 2026.

Mapu (Figure1) akuonetsa m'mene kunazizilira madera osiyanasiyana m'sabata yangothayi pofananizira ndi mlingo okhazikika wa kuzizira wa mwezi wa July.





*Figure 1: M'mene kunazizilira m'sabatayi nthawi ya usiku poyerekeza ndi mlingo okhazikika wa kuzizira mu mwezi wa July.*

### MALANGIZO M'SABATAYI

- Asodzi ndi ena ogwiritsa ntchito nyanja akhale osamala pomwe mphepo ya Mwera ikuomba.
- Kukakhala chifunga tikhale osamala panseu poyendetsa galimoto ndi njinga zamoto.
- Kupewa kugwilitsa ntchito mbaula m'nyumba pamene mawindo ndi zitseko zili zotseka kupewa ngozi

*The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw* **Facebook:** Department of Climate Change and Meteorological Services **WhatsApp**: +265 991 690 061

## UNDUNA WA ZACHILENGEDWE

## NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

Ngati mukufuna kudziwa nyengo ya mdera lanu, pezani **Zanyengo App pa play store**

**Malo otsindikizira: Blantyre** **Yatulutsidwa Lamulungu pa 19 July, 2026**